EXAMINATION NO.:______________________________

**BLANTYRE URBAN DISTRICT MOCK EXAMINATIONS BOARD**

**2021 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATION**

# CHICHEWA

**(Malikisi 100)**

**Subject Number: P032**

**Thursday, 8 July** **Time Allowed: 2 h 15 mins**
**1:00 – 3:15 pm**

**Dzina lanu:** ________________________________________________

**Dzina la sukulu yanu:** __________________________________________

## Malangizo:

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba khumi ndi limodzi.**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi. **Gawo A, B**, **C** ndi **D**.
3. Lembani dzina lanu, nambala ya mayeso ndi dzina la sukulu yanu pamwamba pa tsamba lino.
4. Lembani chimangirizo **Kapena** kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.
5. Lembani yankho la mu **Gawo A** pa mapepala omwe ali kumathero kwa mafunso a mu Gawoli.
6. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.
7. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza lembo lokhonza pafunso lililonse.
8. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
9. Pelekani kwa oyang'anila kulemba mayeso (invijileta) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani Zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| | | | |
| 6 - 45 | | | |
| | | | |

© 2021 BUDME

Turn over

**Gawo A: (**Malikisi 30)

**Langizo:** Yankhani **funso limodzi lokha** mwa mafunso awiri ali mmusiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo **kapena** wa kalata. Mawu a chimangirizo chanu **kapena** kalata yanu asachepera**100** koma asabzole **150**.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu: **Chilengedwe**

Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu.

**Ndime yoyamba**
- Tchulani zinthu zachilengedwe zopezeka m'dera lanu.
- Fotokozani ubwino wa zachilengedwe.

**Ndime yachiwiri**
- Njira zomwe zinthu zachilengedwe zimaonongekera.
- Anthu angasamalire bwanji zinthu zachilengedwe?

**Ndime yachitatu**
- Fotokozani kuipa kowononga zinthu zachilengedwe.
- Udindo wa boma pa katetezedwe ka zachilengedwe.

# KAPENA

**2.** Lembani kalata kwa a malume anu omwe amakhala kutali yowafotokozera za chitukuko chomwe chachitika m'dera lanu.

Mwazina tsatani izi polemba kalata yanu:

**Ndime yoyamba**
- Ndi chitukuko chanji chomwe chachitika m'dera lanu?
- Tsiku, mwezi ndi chaka chomwe chitukukocho chidayamba.

**Ndime yachiwiri**
- Fotokozani momwe chitukukocho chidayambira.
- Mudatenga gawo lanji pantchito yachitukukocho?

**Ndime yachitatu**
- Chitukuko chatukula bwanji dera lanu?
- Zomwe mukuchita kuti chitukukocho chipitirire.

**Mafunso akupitilira/…..**

**Tsamba loyankhirapo**

Mafunso akupitilira/….

**Tsamba loyankhirapo (Continued)**

**Mafunso akupitilira/….**

**Gawo B:** (Malikisi 20)

## KUMVETSA NKHANI

**3.** Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.

### PA BWALO LA MLANDU

Pabwalo pamakhala kanenedwe kake ka mlandu kamene kamatchedwa chowa. Chowachi chimachitika kufuna kuona bwinobwino magwero ake a mlandu popeza kale kunalibe mchitidwe wolemba pamene woyankhula ali kufotokoza. Woweruza anali kubwereza mawu aja amene munthu wofotokoza wanena. Tsono uja wafotokozayu amabuula movomereza ngati wobwereza mawu uja adali kulondola zimene amazifotokozazo.

Pabwalo loweruza mlandu lotchedwa Chakwanu leka, m'mawa wa tsiku Loweruka anthu adali ndi ndi ndi kudikirira a mfumu a Mangani kuti ayambe kuweruza milandu. Dzuwa litakwera pang'ono, mwadzidzidzi anthu onse adaona mfumu Mangani ndi akulu a bwalo a Chitchayo ndi a Chikwekwe akutulukira poteropo kuti balamanthu.

Anthu onse anangoti gwadugwadu mmenemo nkuti Kadalo mtima uli thi thi thi. Mfumu Mangani idali ndi chikaliwo chake utsi uli pha pha pha, tsinya liri kwe ngati wayambana ndi munthu. "E-e-he! Idayankhula mfumu Mangani uku ikukhala pa chitsa cha mtengo koma nthawiyo nkuti akulu a bwalo atakhala kale pansi".

"Chete!" Adatero mkulu wa bwalo a Chikwekwe . "Tsopano mverani mfumu Mangani, nthawi yomweyo anthu onse adakhala chete. Pano monga mudziwa," idatero mfumu potsekulira bwalo lake loweruzira milandu.

"Pano pa Chakwanu leka, pamene mboni ziri kupereka umboni, sindifuma kumazidula mawu ayi. Pamene wina akufotokoza nkhani mmene idayendera, osamagona ndi make khutu yemwe ayi. Ine pomaliza nkhani iliyonse ndidzagamula molingana ndi umboni ndi kakhalidwe ka nkhaniyo". Adatero a mfumu Mangani.
"Tsopano iwe Pinda, imirira yamba kufotokoza dandaulo lako"

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

a. Tchulani dzina la bwalo lomwe a mfumu a Mangani amaweruzirapo milandu.

_______________________________________________

**(malikisi 1)**

b. Ndi udindo wanji omwe a Chikwekwe ndi a Chitchayo adali nawo?

_______________________________________________

**(malikisi 2)**

c. Kodi chowa ndi chiyani?

_______________________________________________

**(malikisi1)**

d. Cholinga chochitira chowa chidali chiyani?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**(malikisi 2)**

e. Kodi mfumu Mangani ndi akulu a bwalo adafika nthawi yanji pa bwalo la milandu?

______________________________________________________________________

**(malikisi 1)**

f. Perekani matanthauzo a mawu awa
   i. magwero______________________________________________________
   **(malikisi 1)**
   ii. chikaliwo ____________________________________________________
   **(malikisi 1)**

g. Kodi ofotokoza mlandu amabuula chifukwa chiyani?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**(malikisi 2)**

h. Perekani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.
   i. dula mawu

   ___________________________________________________________________

   **(malikisi2)**

   ii. gona ndi make khutu yemwe

   ___________________________________________________________________

   **(malikisi 2)**

i. Mukuganiza n’chifukwa chiyani mtima wa Kadulo udali thi thi thi?

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**(malikisi 2)**

j. Ndi chenjezo lotani lomwe mfumu idapereka kwa anthu pamene mboni zikupereka umboni wawo.

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**(malikisi 2)**

k. Fotokozani momwe mfumu Mangani imagamulira milandu yake.

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

**(malikisi 2)**

**Gawo C**: Malikisi 10

Yankhani mafunso onse **awiri** m'gawoli.

**4.** Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.

| | | |
|---|---|---|
| **Nasibeko** | : | Odi! Odi! |
| **Tobiasi** | : | Eee! Fikani, nkwabwino koma? |
| **Nasibeko** | : | Ayi, kunyumbaku kwagwa thambo lakuda, a Najere atsamira mkono. |

**Mafunso**

a. Kodi ndi malonje anji omwe aperekedwa m'kankhanika?

_______________________________________________

**(malikisi 1)**

b. Mawu oti kutsamira mkono akutanthauzanji?

_______________________________________________

**(malikisi 1)**

c. Kodi pamsewu nyale yachikasu imatanthauzanji?

_______________________________________________

**(malikisi 1)**

d. Mnyamata wachi Malawi amayenera kutani akamayankhula ndi munthu wamkulu?

_______________________________________________

**(malikisi 1)**

e. Tchulani njira imodzi yosamalira mabuku a sukulu.

_______________________________________________

**(malikisi 1)**

**5. Kupanga ziganizo**

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa;

a. nkhali _______________________________________________

**(malikisi 1)**

b. zedi _______________________________________________

**(malikisi 1)**

c. popeza _______________________________________________

**(malikisi 1)**

d. langa _______________________________________________

**(malikisi 1)**

e. bi _______________________________________________

**(malikisi 1)**

**Mafunso akupitilira/….**

**Gawo D: (**Malikisi 40)

**Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m'mafunso otsatirawa.**

**Mafunso 6 mpaka 10**: Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**6.** Katangale ndi woipa.
- A. mlumikizi
- B. mvekero
- C. mneni
- D. mperekezi

**7.** Iwo adandilandira mwachikondi.
- A. mfotokozi
- B. muonjezi
- C. dzina
- D. mperekezi

**8.** Tengani makasu ndi zikwanje.
- A. mneni
- B. dzina
- C. mlowammalo
- D. muonjezi

**9.** Ndagula nsapato za amayi.
- A. mvekero
- B. mlowammalo
- C. mlumikizi
- D. mperekezi

**10.** Khalidwe ili loyipa.
- A. muonjezi
- B. dzina
- C. mneni
- D. Mperekezi

**Mafunso11 mpaka 15**: Sankhani ntchito za mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**11.** Elube, namwino watisiya.
- A. dzina loitanira
- B. mwini nkhani
- C. pamthera nkhani
- D. dzina lapadera

**12.** Taona mvuwu, Batumeyo.
- A. dzina loitanira
- B. pamthera nkhani
- C. mtsirizo
- D. dzina loitanira

**13.** Naliyera adali mfumu.
- A. pamthera nkhani
- B. dzina loitanira
- C. mtsirizo
- D. mwini nkhani

**14.** Teleza wapita kumsika.
- A. dzina loitanira
- B. dzina lapadera
- C. mwini nkhani
- D. dzina losonyeza malo

**15.** Petulo wagula njinga.
- A. pamthera nkhani
- B. mwini nkhani
- C. mtsirizo
- D. dzina lapadera

**Mafunso 16 mpaka 20.** Sankhani chachikazi cha mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**16.** Wakunjira afika mochedwa lero
- A. nankungwi
- B. mzidzi
- C. mpongozi
- D. mdzakazi

**Mafunso akupitilira/….**

**17.** Agogo agula <u>mtheno.</u>
- A. mtsibweni
- B. thadzi
- C. nzidzi
- D. nkhosa

**18.** A Molosoni akucheza ndi <u>muphwa</u> wawo.
- A. mfumukazi
- B. mferekazi
- C. mfumukazi
- D. mfumu

**Mafunso 19 mpaka 23. Sankhani mtundu wa muonjezi yemwe watsekedwa mzere kunsi kwake mziganizo zotsatirazi.**

**19.** Yohane amaganiza <u>mwachibwana.</u>
- A. wanthawi
- B. wamuyeso
- C. wochulukitsa
- D. wamachitidwe

**20.** Buluzi ali gone <u>pamwala.</u>
- A. wamuyeso
- B. wamalo
- C. wamchitidwe
- D. wochulukitsa

**21.** <u>Makedzana</u> kunalibe ana amwano.
- A. wanthawi
- B. wamalo
- C. wamuyeso
- D. wofunsa

**22.** Gilibati wavulala <u>kwambiri.</u>
- A. wowerenga
- B. wofunsa
- C. wamuyeso
- D. wamalo

**23.** Mwafika <u>bwanji</u> kuno?
- A. wamchitidwe
- B. wochepetsa
- C. wochulukitsa
- D. wofunsa

**Mafunso 24 mpaka 26: Sankhani matanthauzo oyenera a zilapi zotsatirazi.**

**24.** Akazi amakono otaya ufa wosaphika.
- A. chule
- B. nankafumbwe
- C. nkhuku
- D. mphemvu

**25.** Amfumu akakhuta koma kuwamanga.
- A. nzimbe
- B. thumba
- C. mtolo
- D. Nkhuni

**26.** Kuchigwira nchigwira koma sindichiona.
- A. nkhongo
- B. chala
- C. mwendo
- D. phazi

**Mafunso 27 mpaka 31.Sankhani msintho wa aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

**27.** Mwana <u>wavula</u> Malaya aja.
- A. wochititsa
- B. wochitirana
- C. wotsutsa
- D. womchitira

**28.** Botolo ilo <u>lasweka.</u>
- A. wochitidwa poyera
- B. wonyazitsa
- C. womchitira
- D. Wochitidwa mchibisira

**Mafunso akupitilira/….**

**29.** Patuma wandichapira zovala.
- A. wochitirana
- B. womchitira
- C. wochititsa
- D. Wotsutsana

**30.** Penyetsetsa kuti uwone bwino.
- A. wochititsitsa
- B. womchitira
- C. wochititsa
- D. wochitirana

**31.** Atsikana awo amenyana molapitsa.
- A. wotsutsa
- B. wonyazitsa
- C. wochitirana
- D. womchitira

**Mafunso 32 – 34. Sankhani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

**32.** Tidapita kutawuni titatha kudya mfisulo.
- A. nkhomaliro
- B. kadzutsa
- C. zakudya
- D. mgonero

**33.** Tadeyo wakwidzingidwa lero.
- A. wanjatidwa
- B. wamasulidwa
- C. wamangidwa
- D. wapezedwa

**34.** Amayi ali ku gomo.
- A. chigwa
- B. phiri
- C. tchire
- D. nkhalango

**Mafunso 35 – 37. Sankhani matanthauzo a zining'a zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

**35.** Azakhali apatsidwa kachipsolopsolo kuti akaponye pakhala.
- A. akawotche
- B. akaphike
- C. akakazinge
- D. akaphe

**36.** Lero kwathu tidyera utaka fumbi.
- A. ngombe
- B. bakha
- C. nkhumba
- D. mbewa

**37.** Ife tidagwira tambala kukamwa mmene timapita.
- A. kuchedwa
- B. kupha tambala
- C. kutenga tambala
- D. Kulawirira

**Mafunso 38 mpaka 40. Sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

**38.** Kuti ndinu aulemu ndi zoona.
- A. yamfotokozi
- B. ya dzina
- C. yoima payokha
- D. yamuonjezi

**39.** Adayima pamene adawona agogo.
- A. yamuonjezi
- B. yoyima payokha
- C. yamfotokozi
- D. yadzina

**Mafunso akupitilira/…**

**40.** Fotokozani malangizo <u>amene namwino adapereka.</u>

A. yoima payokha
B. yamuonjezi
C. ya dzina
D. ya mforokozi

**Mafunso 41 mpaka 43. Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.**

**41.** Mawere awirirana.

A. chikondi chapamudzi
B. atupa kwambiri
C. atulutsa mkaka wambiri
D. kudana pachibale

**42.** Pakadafunda padajiwitsa galu.

A. muvi umalasa okonda kugona
B. Mavuto samayang'ana nkhope
C. Kupeza mavuto chifukwa chakunyozera
D. tizikonda kwambiri anzathu

**43.** Mwezi satungira mkanda

A. anthu sayenda ndi usiku
B. Ntchito zochitika ndi mdima sizilongosoka
C. pali chabwino pali choyipa
D. Kugwira ntchito ndi mwezi

**Mafunso 44 mpaka 45:** Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zamkalembedwe zoyenera mziganizo zotsatirazi.

**44.** A. Kalanga ine. ndiwo zija zapserera.
B. Kalanga ine! ndiwo zija zapserera.
C. Kalanga ine! Ndiwo zija zapserera.
D. Kalanga ine. Ndiwo zija zapserera.

**45.** A. "Ine sindifuna zamasewera," mfumu idatero.'
B. Ine sindifuna zamasewera, mfumu idatero."
C. Ine sindifuna" zamasewera, mfumu idatero.
D. Ine sindifuna zamasewera, "mfumu idatero"

# MAFUNSO ATHERA PANO

**NB: Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba khumi ndi limodzi**

# BLANK PAGE